

Tito : 3:1-15

Mutu : Mpingo uyenera kuchita ntchito zabwino

Ndipereka moni wa Kumwamba kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero Mulungu atitsogolere ndi mau apa Yeremiya 17:13, amene akunena kuti, “Inu Yehova, chiyembekezo cha Israyeli, onse amene akukusiyani Inu adzakhala ndi manyazi; onse ondichokera Ine adzalembedwam'dothi, chifukwa asiya Yehova, kasupe wa madzi amoyo.”

Tsono mupologalamu yapita ija, tinali kusanthula Tito 2:1-15, momwe timakambirana nkhani yakuti mpingo uyenera kukhala ndi chiphunzitso choyenera. Ndipo lero pa Tito 3:1-15, pamene tikutseka buku limeneli, tikambirana nkhani yakuti mpingo uyenera kuchita ntchito zabwino.

Tito 3

Chapter chino ndi chomwe chikuonetsa chithunzi chonse, momwe Mulungu afuna kuti mpingo wake uyendetsedwe mwa ndondomeko yoyenera. Tsono tikunena kuti Mulungu afuna kuti mpingo ukhale ndi chiphunzitso choyenera. Pachifukwa chimenechi, Paulo

akumuuza Tito kuti ayenera kupereka Uthenga momwe muli mau oona, amene ndiwothandiza kupewa kapena kutsutsa chiphunzitso chonama.Ndiye tikuphunzira kuti, mpingo uyenera kuchita zonse zimene Mulungu afuna, kutimpingowouchite kapena ugwire ntchito zabwino. Mwanjira ina tikunena kuti ntchito zabwino ndiwo umboni wa kupulumutsidwa.

M'chapter chimenechi tipezamo mitu isanu ndi umodzi; Poyamba Tito, amayenera kuphunzitsa anthu kukhala womvera ulamuliro pakuti pakutero zimaonetsa mtima wodzichepetsa ndi ulemu kwa anthu amagulu onse. Kachiwiri, Tito ayenera kuphunzitsa kukhala omvera chifukwa iwo, ngati akristu poyamba asanatembenuke mtima anali monga anthu ena onse osamvera ndi woipa, koma tsopano anamasulidwa mwa cholinga cha chokoma cha Mulungu. Kachitatu Tito, akulimbikitsidwa kuti sayenera kuchita mtsutso, mkangano ndi kulimbana pa za lamulo. Kachinayi, Tito akulangizidwa kuti ayenera kutaya munthu aliyense wotsutsa chiphunzitso choona, atathakumuphunzitsa.Kachisanu tipeza kuti Paulo akumuuza Tito kuti adzenawoZenasi ndi Apollo ku Nipoli.Ndiye poumbamkota zonsezi, tipeza kuti Tito, amayenera

kuphunzitsa makhalidwe a Kristu m'dziko komanso momwe angakhalire ndi anthu otsutsa Uthenga Wabwino.

1. Uwakumbutse iwo agonje kwa akuru, ndi aulamuliro, akhale omvera, okonzeka pa ntchito iri yonse yabwino;

Paulo mundime ino, akulangiza Tito kuti mpingo uyenera kukhala ndi anthu amene ndi womvera ulamuliro. Kunena kuti mkristu ayenera kumvera malamulo a dziko momwe iye akhala, pokha-pokha ngati malamuliwo akulepheretsa udindo ndi kukhala paubale ndi Mulungu. Koma chimakhala chinthu chokhumudwitsa kuona anthu wokhulupirira akuchita zinthu mwadalamophwanya malamulo a dziko. Tere ndichifukwa chake pa Aroma 13:1, Paulo akunenetsa kuti, “Anthu onse amveremaulamulo a akulu; pakuti palibe ulamuliro wina koma wochokera kwa Mulungu; ndipo iwo amene alipo aikidwa ndi Mulungu.” Kutsimikiza kuti mkristu ayenera kumvera malamulo onse amene satsutsana ndi mau a Mulungu. Kutsindika kunena kuti wokhulupirira ayenera kukhala wokonzeka kuchita chinthu chilichonse chabwino, chomwe angathe kuchita. Kunena kuti mkristu sayenera kuumilizidwa kuchita

chinthu chabwino ayi, koma achiyese mwayi kuchita chinthu chabwino.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani pano ikunena kuti akristu ayenera kukumbutsidwa kuti ayenera kukhala zitsanzo pakumvera ulamuliro wonse umene uli pa iwo. Kutanthauza kuti kufuna kukhala paufulu, kuyenera kuchitika mwanzeruyotsogozedwa ndi mau a Mulungu. Kunena kuti kukhala ndi mwayi wokhala mkristu, sizitanthauzakufooketsa kapena kuleka udindo wa munthu ku Boma ayi. Koma uyenera kukhala mwayi wolimbikitsakumvera ulamuliro.

Kutsimikiza kuti mkristu ayenera kukhala wokonzeka kuchita china chilichonse chomwe chingalemekezetse chipembedzo. Awa, ndiwo mau a Paulo pa Afilipi 4:8, amene akuti, “Chotsalira, abale, zinthu ziri zonse zoon, ziri zonse zolemekezeka, ziri zonse zolungama, ziri zonse zoyera, ziri zonse zokongola, ziri zonse zimveka zokoma; ngati kuli chokoma mtima china, kapena chitamando china, zilingirireni izi.” Kutanthauza kuti kukhala munthu wantendere, wofatsa ndi wolankhula mau okoma,

sizokwanira pa izo zokha, popanda kuchita ndi kuonetsa ntchito zabwino.

2. Asachite mwano munthu ali yense, asakhale andeu, akhale aulere, naonetserechifatso chonse pa anthu onse.

Tito akuuzidwa kuti aphunzitse kuti mkristu, sayenera kuononga dzina la munthu wina. Kutanthauza kuti mkristu sayenera kunenera munthu wina zoipa ayi. Kutsindika kuti inu ndi ine ngati akristu, sitienera kunena nkhani ya munthu wina yomwe tikuona kuti ikhoza kumuonongera dzina kapena kumunenera nkhani yonama ayi. Mwanjira ina tikunena kuti wokhulupirira aliyense ayenera kulankhula kwa munthu mnzake komanso za iye mwanjira yakuti sayenera kudandaula kuti tamuonongera mbiri yake ayi.

Nkhani ikulinga pakuti nthawi zina inu ngati mkristu mukhoza kufunsidwa kupereka umboni wazinthu zomwe mudziwa pamnzanu. Apa, inu muyenera kunena chinthu chilichonse choona, tiyenera kuchita chimenechi, osati ndi cholinga chofuna kumupweteka kaya kuti ife tikondwerenazo ayi. Kutsindika kunena kuti chinthu chilichonse chomwe munganene chiyenera kukhala choona ndi chilungamo. Inu ndi ine, tiyenera kuyesetsa kupewa

kuonjezera nkhani kuti imveke bwino. Sitiyenera kusintha cholinga cha mzathu ndi kuikamo cholinga chathu, popeza sitidziwa cholinga chake. Pachifukwa chimenechi, tiyenera kuyesetsa kukhala anthu osakangana ndi anthu ena. Uku, ndikukwaniritsa mau apa Afilipi 4:5, amene akuti, “Kufatsa kwanu kuzindikirike ndi anthu onse. Ambuye ali pafupi.” Mwa ichi, mkristu ayenera kutsanza Kristu amene ali chitsanzo chathu chokoma. Koma ngati mpingo wapeza anthu ena kuti ndiwo sakuchita zinthu zabwino, uyenera kuwatchula mayina awo monga muja adachitira Paulopotchulamaina a Figelo, Alesandrowosula komanso Dema, amene adamusiya, nakonda zinthu za dziko. Ndiye mwa mau onsewa tikuphunzira kuti udindo wa mkristu kwa anthu onse, ndikuonetsa zotsatira za kuchuluka kapena kukwanira kwa chisomo cha Mulungu.

3. Pakuti kale ifenso tinali opusa, osamvera, onyengeka, akuchitira ukapolo zilakolako ndi zokondweretsa za mitundu mitundu, okhala m’dumbo ndi njiru, odanidwa, odana wina ndi mnzake.

Paulo pano akuonetsa chithunzi cha momwe munthu wosatembenuka mtima ali, komanso ndi momwe ife tinali tisanatembenuke mtima. Taonani kunenetsa kuti inu ndi ine, kale tisanatembenuke mtima, tinali opusa, osamvera, onyengeka, akuchitira ukapolo zilakolako ndi zokondweretsa zambiri ndi kudana ndi ena. Ichi, ndicho chithunzi cha dziko lotaika m'chionongeko.

Tikunena kuti inu mukhoza kuona makhalidwe amenewam'mabanjayachikunja. Tapitaninso malo a business ndi m'malo ogwira ntchito achikunja, mukapeza zinthu zonsezi. Mwachisoni kuti zinthu zomwezi, zikuonekanso mumpingo, pakati pa wokhulupirira. Tikunena kuti mumpingo momwe muyenera kumaonetsa kuti anthu amakondana, ndimo mukupezeka chinyengo, komanso anthu ndi odzala ndi mtima wachisiriro, udani ndi kuchitiranamiseche. Tere, ndichifukwa chake mu mpingo muli timagulu-timagulu ta anthu, chikhalireniamanena kuti ndiwo amodzi m'chikhulupiriro chawo. Ichi, ndicho chinthu chimene chimanyazitsa dzina la Kristu. Kutsindika kuti chithunzi taonachi, cha makhalidwe achikunja, sichiyenera kukhala

chithunzi cha inu ndi ine, ngati anthu wokhulupirira ayi, popeza ifetinamasulidwakuzinthu zimenezi mwachisomo cha Mulungu. Momwemo, monga Mulungu anatilandiraifem'zoipa zathu, tiyenera ifenso kuchita chimodzi-modzi ndi anzathu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kutsindika pano kuti pamene Paulo akunena kuti ife tinali wopusa, akutanthauza kuti munthu ali ndichilakolako chofuna kuchita chabwino. Ndiye kufuna kuchita zinthu zabwino popanda chisomo cha Mulungu ndi kosatheka. Pachifukwa chimenechi, tikunena kuti palibe chinthu chimene chingathandize mkristu kukhala wodzichepetsa, koma kukhala ndi nthawi yomaona moyo wako wakale. Ichi, ndichimene Paulo akunena kuti ifenso kale tinali wotere. Mwanjira ina Paulo akunena kuti ali pamene ali, chifukwa chakuona zinthu zazikulu zomwe Mulungu anamuchitira. Kutanthauza kuti pa iye yekha sakanatha kufika pamenepa. Kunena kuti sakanatha kupeza chisomo ndi kuyamba kumvetsa zinthu zauzimu. Mwanjira Paulo akunena kuti, ifepatokhatiribe chifukwa choweruzira anthu osatembenuka mtima, popeza tinafumulidwa m'makhalidwe amenewa, osati mwanzeru ndi mphamvu zathu ayi, koma mwa

chifundo ndi chisomo chaulere, cha Mulungu mwa ntchito yomwe anagwira Kristu. Ndiye Yakobo 3:13, akunena kuti, “Ndani ali wanzeru ndi waluso mwa inu? aonetsere ndi mayendedwe ake abwino ntchito zake mu nzeru yofatsa.” Kutsimikiza kuti ndi makhalidwe athu okoma, anthu oipa akhoza kutembenuka mtima. Ichi, ndichimene akunena Yuda 1:23, pamene akuti, “Koma ena muwapulumutse ndi kuwakwatulakumoto; koma ena muwachitire chifundo ndi mantha.”

Ichi, ndichifukwa chake Paulo akunenetsa kuti, aulamuliro onse, ngakhale oipa, tiyenera kuwamveramzinthu zabwino zomwe zigwirizana ndi malamulo. Ndiye akunenanso kuti sipayenerakunenerana zoipa ndipo kuti ife akristu tiyenera kukhala ndi munthu wina aliyense mwamtendere.

4. Koma pamene kukoma mtima, ndi chikondi cha pa anthu, cha Mpulumutsi wathu Mulungu zidaoneka,
5. Zosati zochokera m’ntchito za m’chilungamo, zimene tidazichitaife, komatu monga mwa chifundo chake anatipulumutsa ife, mwa kutsuka kwa kubadwanso ndi makonzedwe a Mzimu woyera.

Paulo akunena kuti chikondi cha Mulungu chinaonekeram'chikonzero cha chipulumutso chathu, pamene tinali muuchimo wadzaoneni. Koma pamene chifundo cha Mulungu chinaonetsedwakwa ife, tinatembenuka kuchoka kuuchimo wathu, tinakhala wokonzeka m'maso mwake. Ichi, chinachitika osati chifukwa cha ntchito zathu zabwino zomwe tinachita, koma chifukwa cha chifundo chake.

Tsono verse 3, ndilomwe likutisonyeza momwe ife tinali, tisanafikepodziwa Kristu. Kutanthauza kuti ndikofunika kudziwa kuti sikokwanirakungokhala ndi mtima wakuti ndinatembenuka mtima, osadziwa kumene tikuchokera, chifukwa tikhoza kumachita zomwe tinali kuchita kale tisanatembenuke mtima. Mwanjira ina tikunena kuti anthu ena, pakuyamba chaka, amanena kuti ali ndi maganizo atsopano, koma kupanga chiganizo cha makhalidwe atsopano sikokwanira kuti mukhale mkristu ayi. Kunena kuti sikokwaniransokungokhazikika pakuchita ntchito zabwino ndi kuyesa kuti ndicho chipulumutso ayi. Koma kukhulupirira kuti tinapulumutsidwa mwa chifundo cha Mulungu, pakupereka mwana wake m'modzi yekha nsembe, pamene anafa pamtanda kulipadipola

machimo athu. Apa, ndipo pamene Mulungu anakwanitsa kupereka chifundo chake pa ife, kuti yense wokhulupirira Mwanayoasataike, koma kuti akhalenawo moyo wosatha. Ndiye tikutsindika kunena kuti Mulungu ndiye wolembera m'chifundo chake, kotero kuti ndichokwanira kupulumutsa aliyense amene akhulupirira kuti Kristu anafera machimo ake. Kodi inu mulinacho chikhulupiriro chimenechi?

Paulo akunena kuti chipulumutso chimenechi chinachitika “mwakutsukamwakubadwanso ndi makonzedwea Mzimu Woyera.” Ndiye pamene tikamba nkhani yakutsuka, tikuona za mkhwate m'Kachisi, momwe anthu amasambamo mapazi awo m'Chipangano Chakale. Tsono kutsuka kumeneku ndikomwe Ambuye Yesu anali kulankhula pa Yohane 3:5, pamene anati, “Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi Mzimu, sakhoza kulowa ufumu wa Mulungu.” Ndiye madzi mundime imeneyi akuimira mau a Mulungu, amene ali ndi mphamvu yakutsuka inu ndi ine. Komanso Mzimu Woyera amagwiritsa ntchito madzi (mau a Mulungu), pakutsuka ndi kuyeretsa munthu woipa. Ichi,

ndichimene Paulo akutanthauza pamene akuti,
“kutsukakwabadwanso ndi makonzedwea Mzimu Woyera.”

6. Amene anatsanulira pa ife mochurukira, mwa Yesu Kristu
Mpulumutsi wathu;

7. Kuti poyesedwaolungama ndi chisomo cha Iyetu,
tikayesedweolowa nyumba monga mwa chiyembekezo cha
moyo wosatha.

Mundime ino, ndifuna tigwire mau akuti “kutsanulira pa ife
mochuruka.” Mau amenewa ndiameneandikumbutsa mau amene
ali pa machitidwe Atumwi 2:17, amene akunena kuti, “Ndipo
kudzali m’masiku otsiriza, anena Mulungu, ndidzathira cha Mzimu
wanga pa thupi liri lonse, ndipo ana anu amuna, ndi akazi
adzanenera, ndipo anyamata anu adzaona masomphenya ndi akulu
anu adzalotamaloto.” Ndiye pamene Paulo akunena kuti Mulungu
anatsanulira pa anthu apa dziko, Mzimu Woyera mochuruka, akuti
akhoza kuwasintha ndi kukhala atsopano. Kutsimikiza kuti
Mulungu muzinthu zonse, amaperekazochuluka. Ndipo
kutiali wokonzekakutipatsa zonse mochuruka koposa momwe
tingapemphe. Momwemonso akunenetsa kuti pamene

tinapulumutsidwa ndi chisomo, tiyenera kukhalanachochiyembekezo chochuruka cha moyo wosatha, chomwe chikulozera wokhulupirira ku chiyembekezo chakubweransokwa Kristu kudzatenga mpingo wake. Kodi inu mulinacho chiyembekezo chakuti Kristu akubwera kudzatenga inu?

8. Okhulupirikamauwa, ndipo za izi ndifuna kuti ulimbitse mau, kuti iwoakukhulupirira Mulungu asamalireakhalebe atsogoleri a ntchito zabwino.

Pano tiyambe ndi mau akuti, popeza munthu anapulumutsidwa mwachisomo, sizikutanthauza kuti asagwire ntchito zabwino ayi. Apa, ndipo pamene ayenera kupitiliza kuchita ntchito zabwino. Ichi, ndichimene Paulo akumuuza Tito, kuti alimbikitse akristu aku Krete kuchita ntchito zabwino kosaleka konse. Kutanthauza kuti pamene munthu watembenuka mtima, Mulungu amafuna inu kuchita ntchito zabwino, koma kuchita ntchito zabwino musanatembenuke mtima ndizo sanzazonyasa pamaso pake (Yesaya 64:6). Kutsindika kunena kuti Mulungu afuna inu kuti mutembenuke mtima, ndipo alibe chidwi ndi ntchito zolungama za munthu wochimwa ayi. Mulungu aliwokonzekakukupulumutsani

popeza anaika kale ndondomeko yopulumutsira inu ndi ine. Kunena kuti Mulungu safuna kuti inu muchite ntchito zabwino kuti mukhoze kupulumutsidwa ayi. Koma pamene mwatembenuka mtima, ndipo pamene afuna kulankhula nanu za ntchito zabwino, mwakutumikira Mulungu kufalitsa Uthenga Wabwino wachipulumutso.

9. Koma pewamafunsoopusa, ndi mawerengedwe a mibadwo ndi ndeu ndi makani a pamalamulo; pakuti sizipindulitsa, ndipo ziri zachabe.

Taonani pano Paulo akunena kuti wokhulupirira ayenera kuteteza chiphunzitso choona, koma sayenera kulowa pampikisano ndi mikangano ayi. Kunena kuti izi, sizingakhudze mtima wa munthu ndi kumuthandiza kudza kwa Ambuye ayi.

10. Munthu wopatukira chikhulupiriro, utamchenjezakamodzi ndi Kawiri umkanize,
11. Podziwa kuti wotereyowasandulika konse, nachimwa, nakhala wodzitsutsa yekha.

Tsono ndifuna tione kuti nthawi zina wokhulupirira amafunsidwa kugwira ntchito pamodzi ndi anthu amene atsutsananawochikhulupiriro. Kunena kuti anthu amene apatukapachikhulupiriro choona. Kawiri-kawiri ndiwo anthu amene amagawa mpingo chifukwa ndiwo amapangitsatimagulutinamumpingomo. Ndiye Paulo akumuuzza Tito kuti, asakhale naye pamodzi munthu wotere, amchotse. Kutsimikiza mau apa Mateyu 18:17, amene akunena kuti, “Ndipo ngati iye samvera iwo, uuze mpingo; ndipo ngati iye samveransompingowo, akhale kwa iwe monga wakunja ndi wamsonkho.” Kutanthauza kuti pamene munthu wopatukayuadzudzulidwakangapondipo kuti safuna kusintha, mpingo uli ndi mphamvuyomuchotsa pofuna kusungachiyero chake, kuti mwina pakulangika, mwa m’dalitso wa Mulungu akhoza kubwerera kuchikhulupiriro choona.

12. Pamene ndikatuma Artemakwa iwe, kapena Tukiko, chita changu kudza kwa ine ku Nikopoli: pakuti ndatsimikiza mtima kugonerako nyengo yachisanu.

13. Zenasinkhoswe ya mirandu ndi

Apoloufulumirekuwakonzeraaulendo kuti asasowe kanthu,

14. Ndipo anthu athu aphunzirensoasunge ntchito zabwino
zofunika, kuti asakhale osabalachipatso.

Paulo pano akulimbikitsabe wokhulupirirakuti ayenera kugwira
ntchito zabwino, kotero kuti ndibwino kukhala ndi chizolowezi
chochita ntchito zabwino. Ntchito zabwino ndizomwe tiyenera
kuphunzira kuchita, popeza sizopepuka ayi.

Ndipo pamene tikumaliza bukuli, Paulo akutsekandim'dalitsokwa
anthu onse, tamvani;

15. Akulankhula iwe onse akukhala pamodzi ndi ine.

Lankhulaotikondawom'chikhulupiro. Chisomo chikhale ndi
inu nonse.

Lero tilekeza pano, komanso tatsiriza bukuli, momwe timasanthula
Tito 3:1-15, pa nkhani yakuti mpingo uyenera kuchita ntchito
zabwino.

Ambuye akudalitseni inu. Amen!

